# Malongosoledwe a coonadi ca m'Baibulo

## Za malamulo a Mulungu

1. Momwe Mulungu anatipatsa malamulo ake
2. Citanthauzo ca malamulo
3. Malamulo a Mulungu ndi abwino
4. Cifukwa cake sitimvera malamulo a Mulungu
5. Zifukwa zake za cilango ca uchimo

Zolembedwa zina za m'bukuli zinasandulidwa kucokera mu buku la 'Schoolland, Marian. M. (1962), *Leading Little Ones To God* (21st ed), Wm. B. Eerdmans Publishing Company.'

© Stephanos Zambia Trust
www.kudziwazamulungu.com

## 1. Momwe Mulungu anatipatsa malamulo ake

*Mulungu wamkulu ndi woopsa – Deuteronomo 7.21b*

**Kuwerenga**
Eksodo 19.16-19

**Malongosoledwe**
Tinaphunzira kuti Mulungu analenga anthu onse. Mulungu ndi Mwini wa anthu onse. Mulungu ndi wanga. Mulungu ndi Mwini wanu. Aliyense ndi wa Mulungu, cifukwa Iye analenga anthu onse.
Tiyenera kukhala miyoyo yathu kwa Iye, cifukwa Iye ndiye Mwini wathu. Tiyenera kumkondweretsa. Tiyenera kukhala m'njira momwe afuna kuti tikhaliremo.
Mulungu anatiuza momwe tiyenera kukhala. Mulungu anatipatsa malamulo ake. Malamulo ake atiuza zomwe tiyenera kucita ndiponso zomwe sitiloledwa kucita. Malamulo ake atiuza kuti anthu a Mulungu ayenera kukhala anthu otani.
Kalekale pamene Aisrayeli anali anthu opatulika a Mulungu, Mulungu anawapatsa Malamulo Khumi.
Aisrayeli anakhala m'mahema. Kunali mahema ambiri ozungulira phiri la Sinai.
Mose anali mtsogoleri wa anthu a Mulungu. Anawatsogolera kucokera ku dziko la Aigupto. Tsiku lina Mulungu anauza Mose, 'Uza anthu kudzikonzera. Ayenera kusamba ndi kucapa zobvala zao. Patapita masiku atatu ndidzatsikira kwa iwo. Ndidzabwera pamwamba pa phiri la Sinai. Ndidzalankhula nao'.
Mulungu sadatsike kulankhula ndi anthu ena. Kuyendera uku kwa Mulungu ndi kwapadera. Aisrayeli analephera kuyembekeza. Anatsuka mahema ao, anasamba ndi kucapa zobvala zao.
Patapita masiku atatu Aisrayeli anapenya pabwalo pa mahema ao m'mawa. Anadabwa momwe Mulungu adzatsika kwa iwo. Anayang'ana phiri la Sinai. Anaona mtambo ukulu wakuda pamwamba pa phiri. Anamva cibvomerezi. Ndipo anaona kunyezimira kwa mphezi mkati mwa mtambo wakuda.
Mose anaitana anthu, 'Bwerani, sonkhanani pafupi ndi phiri!'
Pamene onse anali pafupi ndi phiri, Mulungu anatsika. Anadza m'moto ndi utsi. Phiri linagwedezeka pamene Mulungu anatsikirapo. Anthu anamva mantha. Pa nthawi imeneyo anaona ndi kumva kuti Mulungu ndi wamkulu.
Kenaka anamva mau a Mulungu. Mulungu ananena:

Ine ndine YEHOVA Mulungu wako.

1. Usakhale nayo milungu ina koma Ine ndekha.
2. Usadzipangire iwe wekha fano losema.
3. Usachule dzina la Yehova Mulungu wako pacabe.
4. Uzikumbukira tsiku la Sabata, likhale lopatulika.
5. Uzilemekeza atate wako ndi amako.
6. Usaphe.
7. Usacite cigololo.
8. Usabe.
9. Usamnamizire mnzako.
10. Usasirire kalikonse ka mnzako.

Mau awa ndi Malamulo Khumi. Mulungu mwini anapatsa malamulo awa pamene anali pamwamba pa phiri. Ndipo mau ake anali monga mphezi.
Anthu onse anabwerera kucokera ku phiri. Anamva mantha. Mose anati, 'Osacita mantha. Mulungu akuonetsani ukulu wake kuti muzimumvera'. Ndipo iwo analonjeza kumvera. Anati, 'Tidzacita zonse zimene Mulungu anena'.

**Kukambirana**
1. Kodi Mulungu anapatsa malamulo ake pa phiri liti?
2. Kodi Aisrayeli anaona ndi kumva ciani?
3. Ndi cifukwa ciani Aisrayeli anamva mantha?
4. Ndi cifukwa ciani anthu ayenera kucita zimene Mulungu anena?
5. Kodi mumamvera Mulungu m'moyo wanu?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wamkulu wa Kumwamba, Zikomo kwambiri kuti munatipatsa malamulo anu kuti tidziwa zimene mufuna. Kawirikawiri tilephera kucita cifuniro canu. Ndife ocimwa: anthu amene sakwaniritsa kusunga malamulo anu. Mutione mwa Yesu Kristu amene sanalakwe kucita cifuniro canu. Tikupemphani izi m'dzina lake, Amen.

## 2. Citanthauzo ca malamulo

*Ndipo muzikonda Yehova Mulungu wanu ndi mtima wanu wonse, ndi moyo wanu wonse, ndi mphamvu yanu yonse – Deuteronomo 6.5*

**Kuwerenga**
1 Mafumu 17.8-16

**Malongosoledwe**
Malamulo a Mulungu atanthauza kuti nthawi zonse tiyenera kuika Mulungu patsogolo. Tizikonda Mulungu kuposa munthu wina aliyense. Tizimvera Mulungu tikalibe kumvera wina aliyense. Tiyenera kucita zonse zimene Mulungu afuna kuti ticita. Tizilemekeza Mulungu masiku onse ndi m'zonse zimene ticita.
Baibulo litiuza za mkazi wamasiye wosauka ndi momwe anaika Mulungu patsogolo.
Tsiku lina mkazi wamasiye wosauka anapita kukatola nkhuni. Kunali njala yaikulu m'dziko. Mulungu sanalole mvula kugwa cifukwa anthu anali oipa kwambiri. Ndipo cifukwa kuti kunalibe mvula, kunalibe zomera. Kunalibe mbeu kuti anthu angapange ufa.
Mkaziyo wamasiye wosauka anali ndi ufa waung'ono wotsalapo. Anali kutola nkhuni kuti apange moto kukaumba mkate mogwiritsa nchito ufa uwo waung'ono wotsalapo. Anali ndi mafuta pang'ono kupanga mkate.
Pamene anali kutola nkhuni, mwamuna anabwera pa njira. Iye anali ndi tsitsi lalitali ndi ndevu zazikulu ndipo zobvala zake zinali zadothi.
Mwamunayo anaitana mkazi wamasiye. 'Conde, unditengere madzi'. Mwamunayo anamva kutentha ndipo anakhala ndi ludzu.
Mkazi wamasiye anati, 'Ee, ndidzakutengerani madzi ang'ono'.
Koma pamene anapita kukatenga, mwamunayo anamuitananso, 'Unditengerenso kanthongo ka mkate!'
Pamenepo mkazi wamasiye anaoneka wosakondwa. 'Ndiribe mkate uliwonse', anati mkaziyo. 'Ndiri ndi ufa waung'ono ndi mafuta pang'ono cabe. Nasonkha moto kuti tipange mkate wa ine ndi mwana wanga wamwamuna. Zitatha izo tifunika tife.'
Mwamunayo anati, 'Musacite mantha. Pita kukapanga mkate wanu. Koma poyamba undipangire kamkate kwanga. Kenaka mudzapanga mkate wa inu ndi mwana wanu wamwamuna. Mulungu akamba kuti mudzatsalabe ndi ufa ndi mafuta. Nthawi zonse udzatsala ndi ufa ndi mafuta mpaka mvula idzabwera ndi zinthu zidzameranso.
Mwamunayo anali meneneri wa Mulungu. Anachedwa Eliya. Pamene mkazi wamasiye anamva mau a Eliya, iye anapita kupanga mkate. Ndipo anabweretsa kamkate kang'ono kwa Eliya. Mkaziyo anali ndi njala ndipo mwana wake wamwamuna analinso ndi njala, koma anapatsa mkate woyamba kwa Eliya cifukwa Eliya anali munthu wa Mulungu. Anaika Mulungu poyamba. Anakhulupirira mau a Mulungu olankhulidwa ndi Eliya ndipo anamumvera.
Mulungu anadalitsa mkazi wamasiye wosauka. Anapanga mkate nthawi zonse pamene iye, mwana wake wamwamuna ndi Eliya anafunika cakudya. Ndipo nthawi zonse kunatsalako ufa waung'ono ndi mafuta pang'ono, monga Mulungu adalonjeza.

**Kukambirana**

1. Kodi malamulo a Mulungu atanthauza ciani?
2. Kodi mkazi wamasiye anaonetsa bwanji kuti anakonda Mulungu?
3. Fotokozani momwe tingaike Mulungu poyamba m'zitsanso izi:
    a. Pamene alendo afika ku nyumba yathu pa Sondo pa nthawi ya kupita ku calichi
    b. Pamene anthu afuna kuti tipempha ng'anga thandizo lake
4. Patsani zitsanzo ziwiri za m'miyoyo yanu za kuika Mulungu patsogolo.

**Citsanzo ca pemphero:**
Mulungu wathu wa Kumwamba, Tithandizeni kusunga malamulo athu ndi kukuikani patsogolo nthawi zonse. Uchimo wa m'mitima yathu ndi yolimba kwambiri. Tipatseni mitima yokukondani moonadi. Tikupemphani izi m'dzina la Yesu Mpulumutsi, Amen.

## 3. Malamulo a Mulungu ndi abwino

*Mau anu ndiwo nyali ya ku mapazi anga, Ndi kuunika kwa panjira panga – Salimo 119.105*

**Kuwerenga**
2 Mafumu 23.1-3

**Malongosoledwe**
Kodi ndinu osangalala pamene simumvera? Iai, kukhala osamvera sikungapangitse anthu kukhala okondweradi. Kusamvera malamulo a Mulungu sikungapangitsenso anthu kukhala okondweradi.
Ngati tifuna kukhala okondwera, tiyenera kumvera malamulo a Mulungu. Tiyenera kukonda Mulungu ndi kudziwa kuti atikonda.
Mulungu anatipanga ku ulemerero wake, sitero kodi? Ndipo sitingakhale okondwera pokhapo timkondweretsa Mulungu. Ndife okondwera cabe pamene tiri monga Iye afuna kuti tizikhala.
Kodi mumakondwera pamene amai anu akukwiyirani? Iai! Koma mwakondwera pamene amai anu asangalatsidwa ndi inu. Cimodzimodzi ndife okondwera pamene Mulungu asangalatsidwa ndi ife. Cifukwa cake tiyenera kumvera malamulo ake.
Ndipo kuli cifukwa cina ca kumvera malamulo a Mulungu. Ngati sitimvera, Mulungu adzatipatsa cilango. Ayenera kutilanga cifukwa ici ndi coyenera.
Kalekale kunali mnyamata wamng'ono wochedwa Yosiya. Baibulo litiuza kuti iye anali mwana wa mfumu. Amoni, tate wake anali mfumu wa Aisrayeli, anthu a Mulungu. Amoni anali mfumu yoipa. Sanamvere Mulungu. Mafumu ena amene adalamulira asanalamulire Amoni analinso oipa. Sanakonde Mulungu ndipo sanampembedze m'Kacisi yake. Iwo anapembedza mafano. Ndipo anaphunzitsa anthu onse kupembedza mafano.
Tsiku lina mfumu yoipa Amoni anaphedwa. Yosiya anatenga ufumu wa tate wake. Anafunika kukhala mfumu.
Yosiya anali mnyamata wa zaka zocepa: zaka zisanu ndi zitatu (8) cabe. Koma pamene anapangidwa kukhala mfumu, iye anati, 'Sindidzakhala mfumu yoipa. Ndikonda Ambuye. Ndidzamtumikira Iye'.
Ndiye Yosiya anauza anthu onse kutaya mafano onse. Anafuna kuti azitumikira Mulungu.
Tsiku lina Yosiya anatuma amuna ena ku Kacisi ya Mulungu. 'Konzani Kacisi ndi kuitsuka kuti tidzatumikiranso Mulungu m'Nyumba yake.
Amuna anapita kukagwira nchito. Anapeza zinyalala zambiri m'Kacisi. Anapeza zitseko zoonongeka ndi zibowo m'zipupa.
Tsiku lina mwamuna anathamanga ku nyumba ya mfumu Yosiya. 'Onani cimene ndapeza!' anati mwamunayo kwa mfumu. 'Buku lakale! Linali pa zodetsa m'Kacisi!'
'Ndiwerengereni', ananena mfumu Yosiya.
Mwamunayo anatsegula buku nayamba kuwerenga. Mfumu Yosiya anamvera. Cimene anamva cinali cabwino komanso cocititsa mantha. Bukulo linali la malamulo a Mulungu. Linasowa. Kulimvanso patapita nthawi yaikulu yosowa kunali kodabwitsa. Koma, ooo, bukulo lifotokoza zinthu zoipa zimene zidzacitika pamene anthu a Mulungu apembedza mafano!
Mfumu Yosiya anaimirira mofulumira. 'Ooo, tacimwira Mulungu kwambiri', Iye anati. 'Sitinamvere malamulo ake! Tidzalangidwa! Kaitana anthu anga onse ndipo wawerengereni bukulo!'
Anthu onse anabwera namva malamulo a Mulungu. Anamva kuti Mulungu adanena kuti adzawalangadi pamene anthu apembedza mafano. Pamenepo anamva cisoni pa macimo ao. Anauza Mulungu kuti adzamtumikira momwe Iye afuna. Malamulo anawauza kukondweretsa Mulungu kotero kuti sadzalangidwa. Malamulo anawathandiza kukhala acilungamo.

**Kukambirana**
1. Ndi ciani cimene citipangitsa kukhala okondweradi?
2. Ndi ciani cimene cidzacitika pamene sitimvera Mulungu?
3. Kodi malamulo a Mulungu ndi abwino kwa ife m'njira yotani?
4. *Wotembereredwa aliyense wosakhala m'zonse zolembedwa m'buku la cilamulo, kuzicita izi*. (Agalatia 3.10) Ndime iyi itanthauza kuti onse olephera kucita cifuniro ca Mulungu ndiwo otembereredwa, angakhale acimwa kamodzi cabe. Kodi mukwaniritsa kumamvera Mulungu?
5. Anthu sakwaniritsa kukhala momwe Mulungu afuna nthawi zonse. Yankho lenileni la uchimo ndilo Yesu Kristu wopacikidwa. *Kristu anatiombola ku temberero la cilamulo, atakhala temberero m'malo mwathu.* Fotokozani ndime imeneyi.

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu Atate wa Kumwambamwamba, Tikuyamikani kaamba ka malamulo anu omwe atiuza zimene tizicita. Tithandizeni kukhala okukondweretsani. Tikupemphani izi m'dzina la Yesu Mpulumutsi, Amen.

## 4. Cifukwa cake sitimvera Mulungu

*Palibe mmodzi wakucita bwino, nnena mmodzi – Salimo 53.3b*

**Kuwerenga**
Salimo 130

**Malongosoledwe**
Kukhala mtsikana wacilungamo kapena mnyamata wacilungamo ndi kwabwino, sitero kodi? Pamene mukhala acilungamo ndinu okondwera: mungaimbe, mungajumphe ndi kusewera. Koma pamene ndinu osamvera, aliyense akumva cisoni. Amai akhala acisoni, atate akhala acisoni ndipo inunso mukhala acisoni. Cikondwerero conse catha.
Ndi cifukwa ciani simukhala acilungamo nthawi zonse kodi? Inde, kukhala acilungamo nthawi zonse ndi kobvuta. Ngakhale anthu akulu sakwaniritsa kukhala acilungamo nthawi zonse. Ndi cifukwa ciani kukhala acilungamo ndi kobvuta kodi?
Kukhala acilungamo nthawi zonse ndi kobvuta cifukwa m'mitima yathu muli uchimo. Kodi mukumbukira nthano ya Adamu ndi Hava? Satana anabwera kwa Hava ndi kumuuza kuti asamvere Mulungu. Ndipo Hava sanamvere Mulungu. Iye ndi Adamu anadya cipatso coletsedwa. Pamenepo uchimo unabwera pa dziko lapansi. Uchimo unaononga kukongola kwa dziko lapansi la Mulungu. Kucokera pa nthawi iyo mwana aliyense abadwa ndi uchimo m'mtima wake. Mnyamata aliyense ndi mtsikana ali nao mtima wocimwa. Ndipo akulu alinso nayo mitima yocimwa.
Kodi mukumbukira cifukwa cake Mulungu anatilenga? Anatilenga kuti tizimkonda, tizimlemekeza ndi kukhala miyoyo yathu kwa Iye. Ndipo atiuza kuti tidzakhala okondwera ngati timkonda, timumvera ndi kumlemekeza.
Koma uchimo umalankhula motsutsa m'mitima yathu. Uchimo utiuza kusamvera. Uchimo m'mitima yathu utipangitsa kukhala okwiya ndi odzikonda. Uchimo umaika kusewera, kukhala okondwera ndi zinthu zina patsogolo ndipo timaiwala kuika Mulungu patsogolo. Malamulo a Mulungu anena kuti tiyenera kukonda Mulungu koposa. Mitima yathu imanena, 'Ine poyamba'. Malamulo a Mulungu anena kuti tiyenera kukonda wina ndi mnzake. Koma sitikondana moyenerera. Ndife odzikonda.
Kudzikuza ndi koipa. Kukhala okwiya ndi koipa. Kunena mabodza ndi kuba ndi koipa. Kusamvera amai ndi atate ndi koipa.
Zinthu zoipa zimakhala munsi m'mitima yathu. Maganizo oipa acokera munsi mwa mitima yathu. Cifukwa cake ticita zimene ife tifuna m'malo mwa kucita zimene Mulungu kapena atate ndi amai athu afuna. Uchimo ndi wamphamvu kwambiri m'mitima yathu. Nthawi zina Satana angalankhule motsutsa m'mitima yathu ndipo atiuza kucimwa monga anauza Hava kucimwa.
Kuganizira uchimo wamphamvu munsi m'mitima yathu
Kuganizira kuti uchimo ndi wamphamvu munsi m'mitima yathu ndi kuti anthu onse acimwira Mulungu kutipangitsa kukhala osakondwa.

**Kukambirana**

1. Ndi cifukwa ciani tiyenera kukhala acilungamo?
2. Ndi cifukwa ciani kukhala acilungamo ndi kobvuta kwa anthu onse?
3. Ndani amene akwaniritsa kutipangitsa kukhala acilungamo kodi?
4. Tiwerenga m'Akolose 2.10a, 'Ndipo muli odzazidwa mwa Iye'. Njira yeniyeni yokhala acilungamo ndi mwa Yesu Kristu, Mwana wa Mulungu. Kodi ndinu mwa Iye?

**Citsanzo ca pemphero**
Ambuye Mulungu, mutipatse mitima yoyera kuti tikhale miyoyo yathu kwa Inu. Tithandizeni kukhala omvera ndi olungama mwa Yesu. Si ndife olungama mwa mphamvu yathu, cifukwa mitima yathu ndi yocimwa. Mutimvere cifukwa ca Yesu Kristu wolungama. Amen.

## 5. Zifukwa zake za kulangidwa kwa uchimo

*Pakuti mphoto yace ya uchimo ndi imfa – Aroma 6.23*

**Kuwerenga**
Genesis 8.6-16

**Malongosoledwe**
Kodi amai anu akupatsani cilango nthawi zina? Kapena atate anu akulangani?
Ndi cifukwa ciani amai kapena atate anu apatsa cilango? Pamene musamvera mufunika kulangidwa. Amai amapatsa cilango cifukwa ico ndi coyenera. Kusamvera konse kufunika kulandira cilango.
Ndipo kuli cifukwa cina. Amai kapena atate akupatsani cilango kuti mukhale olungama. Cilango cimatithandiza ife kuleka zoipa, si tero kodi? Kotero cilango ndi cabwino. Cilango ndi cabwinonso ku anthu akulu. Cilango cimatithandiza kuphunzira kukhala umoyo wosangalatsa Mulungu.
Mulungu ndiye woyera. Kodi mukumbukira kuti angelo amamlemekeza mwa kuimba 'Woyera, woyera, woyera'? Mulungu alibe chimo lirilonse. Iye ndiye woyera ndi wacilungamo. Afuna kuti ifenso tizikhala woyera ndi olungama. Afuna kuti tifanana naye. Mulungu sangatilole kucita coipa kopanda kutilanga, cifukwa Iye ndiye woyera kwambiri. Tikamcimwira tiyenera kulandira cilango.
Pamene sitimvera atate athu kapena amai athu tawacimwira. Koma tikacita tero tacimwiranso Mulungu, cifukwa Mulungu auza ana kuti ayenera kumvera makolo ao. Chimo ndi loipa kwambiri-mbiri.
Uchimo unabwera pa dziko lapansi pamene Adamu ndi Hava anacimwa. Kodi mukumbukira zimene zinacitika? Kucokera pa nthawi iyo uchimo unakula koposa. Posacedwa kunali anthu ambiri pa dziko lapansi ndipo iwo anali oipa kwambiri.
Mulungu anali wacifundo kwa iwo. Sanawapatse cilango nthawi yomweyo. Anayembekeza nthawi yaitali. Anafuna anthu kubwereranso kwa Iye ndi kumtumikiranso.
Koma tsiku lina, pamene Mulungu anayang'ana pa dziko lapansi, anaona banja limodzi cabe limene anayesadi kukhala olungama ndi kumtumikira. Ilo linali banja la Nowa. Anthu ena onse anali oipa kwambiri. Anapanga dziko lokongola la Mulungu kukhala malo oipa.
Mulungu anati, 'Ndidzaononga anthu onse a pa dziko lapansi. Ndidzacotsa zoipa zao zonse.'
Mulungu anauza kuti adzatumiza mvula lalikulu kudzadza dziko lonse lapansi ndi madzi. Ndipo anauza Nowa kupanga combo, ndico cingalawa cacikulu. Ico cinayenera kuoneka monga nyumba. Cinayenera kukhala monga nyumba ya tsanja ndiponso kukhala ndi citseko ndi dzenera.
Nowa ndi ana ake anagwira nchito molimba popanga combo. Ndipo anauza anzao za cigumula. Koma kunalibe amene anakhulupirira kuti cigumula cidzabweradi.
Anatsiriza kupanga combo. Nowa ndi banja lake analowamo, pamodzi ndi nyama zonse zimene Mulungu anafuna kupulumutsa. Kenaka Mulungu anatumiza cigumula. Madzi anali ponseponse pa dziko lapansi. Anthu oipa onse anafa. Iwo okhala m'combo cabe anapulumuka.
Ico cinali cilango coipa kwambiri.
Koma Baibulo likamba kuti chimo lirilonse liyenera kulangidwa ndi cilango coipa: macimo anu ndiponso macimo anga ayenera kulangidwa. Baibulo likamba kuti ocimwa onse amene sabwereranso kwa Mulungu adzatayika ku nthawi zosatha.

**Kukambirana**

1. Ndi cifukwa ciani cilango ndi coyenera ndi cabwino?
2. Kodi Mulungu angatipatse cilango cotani?
3. Mulungu anapulumutsa banja la Nowa mwa cisomo. Kodi cisomo ndi ciani?
4. Ndi cifukwa ciani anthu osalapa ayenera kukhala ku Gehena?
5. Yesu anafa pa mtanda kusenza cilango ca uchimo. Kodi anasenzanso cilango ca macimo anu?

**Citsanzo ca pemphero**
Mulungu wa Kumwambamwamba, Inu ndinu woyeradi. Mulibe chimo lirilonse. Koma ife tiri ndi macimo ambiri cifukwa ca mitima yathu yocimwa. Tiyenera kulangidwa cifukwa ca uchimo wathu. Ngakhale ngati tiyesa kusiya uchimo, tipeza uchimo m'mitima yathu. M'Baibulo tiwerenga kuti Yesu akwaniritsa kuyeretsa ku macimo. Mutiyeretsenso masiku onse kuti tizikhala olungama pa maso panu. M'dzina la Yesu tikupemphani izi, mwa cisomo. Amen.